Kodi muyenera kutani ngati mukukayikira kuti anthu ena akuzembetsa katundu?

Ngati mukukayikira kuti anthu ena akuzembetsa katundu muyenera kukanena ku office ya MRA kapena Polisi yomwe muli nayo pafupi. Mukhozanso kuimba foni mwaulere komanso mwachinsinsi pa **847** pogwiritsa ntchito nambala yanu ya **Airtel, Access** kapena **TNM.** Chomwe muyenera kuchita ndi kupereka nambala ina iliyonse yokwanira zinthu zinayi monga **2031** kapena **5012** ndipo fotokozani popereka umboni momwe zakhalilira. Mukakhala kuti umboni wanu munapereka unapangitsa kuti MRA itolere msonkho inu omwe ukanataika mudzapatsidwa mphoto kuyambira **K5, 000** mpaka **K500, 000** malingana ndi kuchuluka kwa msonkho watoleredwa.

Ngati munthu ozembetsa katundu akukupemphani kuti mumuthandize kunyamula kapena kusunga katundu, kanani chifukwa kuchita izi ndi mlandu.

Ngati mungathandize munthu yemwe akuzembetsa katundu, pompatsa malo ogona kapena kumunyamulira katundu wake ndiye kuti mukuthandiza polibera Boma ndalama zomwe zinakatha kugwira ntchito zina za chitukuko. Dziwani kuti kuthandiza munthu kuzembetsa katundu ndiye kuti mukumupangitsa munthuyo kuti akhale olemera pomwe inu mukusowa chitukuko monga, sukulu, misewu ndi zipatala, mwa zina, kudera lanu ndikumasauka.

Produced by Corporate Affairs Division - MRA

Malawi Revenue Authority
Msonkho House
Independence Drive
Private Bag 247
Blantyre

Tel: +265 - 1 822 588
Fax: +265 - 1 822 302
E-mail: mrahq@mra.mw
Web: www.mra.mw

Develop Malawi, Pay Taxes

Kumvesetsa Za...

KUIPA KOZEMBETSA KATUNDU (SIMAGO)

KODI UDINDO WANU POTHETSA MCHITIDWE WOZEMBETSA KATUNDU NDI WOTANI?

Kodi simago ndi chiyani?

Simago ndi mchitidwe wozembetsa katundu kuchokera kunja kubweretsa mdziko muno kapena kutulutsa katundu mwachinyengo komanso posadzera pa boda. Kuzembetsa katundu kumachitika mnjira zosiyanasiyana monga izi:

- Kuonetsa katundu ochepa pa boda wina nkubisa
- Kupereka malisiti kapena mapepala onama ndi cholinga chofuna kulipira msonkho wochepa kapena kusalipira kumene
- Kudutsitsa katundu njira za mtchire posadzera pa boda

Kodi kuipa kwa simago kapena kuzembetsa katundu ndi kotani?

Kuipa kwa simago ndi uku:

- Boma silitolera msonkho woyenera pa chifukwa ichi chitukuko cha dziko chimalowa pansi
- Simago imapangitsa kuti katundu osaloledwa monga mfuti, mabomba, mankhwala wosokoneza bongo kapena katundu wotha mphamvu (expire) alowe mdziko muno ndikuika miyoyo ya anthu pa chiwopyezo

Munthu atha kutengeredwa ku khoti ndipo akapezeka wolakwa amatsekeledwa kundende ndi kukagwira ukaidi wakalavula gaga kopitilira zaka zitatu

- Makampani ena atha kutsekedwa chifukwa katundu wasimagoyo amagulitsidwa pa mtengo wotsika kamba koti sanalipiridwe msonkho pa boda
- Boma silimatha kupanga kalondolondo woyenera pa katundu amene akulowa mdziko muno ndipo izi zimapangitsa kuti Boma lipange ndondomeko zosayenera za chuma cha dziko lathu

Nanga chilango cha kuzembetsa katundu ndi chotani?

- A MRA amalanda katunduyo ndikumusunga mpaka ataomboledwa
- Munthu amauzidwa kuti alipire chindapusa chosachepera MK100,000 kapena katatu mtengo wakatunduyo kapena kuposera apo
- Munthu atha kutengeredwa ku khoti ndipo akapezeka wolakwa amatsekeledwa kundende ndi kukagwira ukaidi wakalavula gaga kopitilira zaka zitatu